
CHIKALATA CHA PA DZIKO LONSE CHOKHUDZA KUCHITIRA CHILUNGAMO ANA

20 November 2021

Msonkhano Wa Pa Dziko Lonse wa Chaka cha 2021 Wokhudza Kuchitira Chilungamo Ana;

Pamsonkhanowu panafika anthu a mibadwo yosiyanasiyana opitirira 4,800 ndipo anali ochokera m'mayiko oposa 100. Msonkhanowu unayamba pa 15 mpaka 20 November 2021 ndipo unachitika kudzera pa intaneti, pa mutu wakuti "Kuonetsetsa kuti ana onse akuchitiridwa chilungamo: kukonza zoti ana asamasalidwe komanso kuti ena azitenga nawo gawo pankhani zochitira chilungamo ana";

Msonkhanowu unakonzedwa ndi bungwe la Global Initiative on Justice With Children (momwe mukupezeka mabungwe monga *Terre des hommes*, *Penal Reform International*, *International Association of Youth and Family Judges and Magistrates*, komanso bungwe loona za maufulu a ana la *International Institute for the Rights of the Child*) ndi kutsogoleredwa ndi khoti lalikulu la m'dziko la Mexico la *Mexican Supreme Court of Justice*, ndi thandizo lochokera ku bungwe loona za ana la Unicef, ofesi ya oyimira mkulu wa bungwe la *United Nations* pa nkhani za nkhazi zochitira ana, ofesi ya UN pa nkhani za mankhwala ozunguza bongo ndi umbanda, ofesi ya UN pa nkhani ya maufulu, bungwe loona za mgwirizano ndi chitukuko pa chuma la Organisation for Economic Co-operation and Development, komanso bungwe la *Pathfinders for Peaceful, Just and Inclusive Societies*; ndi thandizo lina lochokera ku Council of Europe komanso nyumba ya malamulo ya ku Europe; Baker McKenzie; Scientific Committee, *Committee of Honour*, Child and Youth Advisory Group, komanso misonkhano ya m'mayiko ndi m'mzigawo yokonzekera msonkhano wa dziko lonsewu;

Unatsimikizira za kudzipereka ndi mtima wonse pofuna kupititsa patsogolo, kutetezera, ndiponso kukwaniritsa maufulu a ana motsatira zimene bungwe la UN pa maufulu a ana wotchedwa *UN Convention on the Rights of the Child* ndi mfundo zina zokhudza maufulu a ana pa dziko lonse;

Unakumbutsa anthu mfundo zopezeka mu *Paris Declaration* (wochitikira ku France, m'mwezi wa May 2018), *Geneva Declaration* (ku Switzerland, January 2015), ndiponso *Lima Declaration* (ku Peru, November 2009), zomwe zidamangidwa pa misonkhano itatu ya dziko lonse ya m'mbuyomu yomwe mitu yake idakhudza kupeza chilungamo cha ana, kuonetsetsa kuti chilungamo chikuchitika, komanso kulimbikitsa ndondomeko zoonza chilungamo cha ana;

Kugwirizana ndi mfundo zolembedwa m'chikalata cholimbikitsa anthu kuti achitepo kanthu cha *ku msonkhano wa chilungamo cha ana* (September 2019) chomwe chidalembedwa ndi bungwe la Pathfinders for Peaceful, Just and Inclusive Societies mogwirizana ndi Cholinga cha chitukuko chokhazikika (SDG) cha 16, chomwensho chidapangidwa ndi kuvomerezedwa ndi a mabungwe ambiri a boma komanso omwe si a boma, ndiponso sukulu zosiyanasiyana pa dziko lonse, m'zigawo, ndi m'mayiko;

Kuzindikira kufunika kotsindikanso zofuna za ana ndi achinyamata zimene zidanenedwa pa msonkhano waukulu wa dziko lonse wa m'mbuyomu (ku France, m'mwezi wa May 2018); kufunika kwa mfundo zotsogolera zopezeka mu *kafukufuku wa UN pa dziko lonse pa nkhani ya ana olandidwa ufulu* (November 2019); zotsatira za mliri wa COVID-19 pa nkhani yoti ana apeze chilungamo, malinga ndi chikalata cha bungwe la UN cha ndondomeko zogwirira ntchito, chotchedwa *UN Policy Brief: Mmene mliri wa COVID-19 wakhudzira umoyo wa ana* (April 2020) ndiponso uthenga wochokera ku bungwe la nthambi zosiyanasiyana la *Interagency: Mliri wa COVID-19 ndi Ana Wolandidwa Ufulu* (April 2020); mfundo zofotokozedwa mu chikalata cha UNICEF chotchedwa *Kupeza Chilungamo cha Ana mu nyengo ya mliri wa COVID-19: Maphunziro opezeka ku madera* (December 2020); ndi mfundo za kudzipereka pa nkhani ya ana zoperekedwa ndi atsogoleri a mayiko, nduna za boma komanso akuluakulu oyimira mayiko ku bungwe la UN mu kulengeza kwa ku Kyoto pa nkhani yopititsa patsogolo kupewa umbanda, chilungamo ndi mphamvu ya lamulo, Kyoto Declaration on Advancing Crime Prevention, Criminal Justice and the Rule of Law (Japan, March 2021), pa nthawi ya msonkhano waukulu wa UN wa nambala 14 pa ntchito yopewa umbanda ndi kupeza chilungamo;

Anakambirana mfundo zotsatirazi:

1. Ngakhale kuti bungwe la UN loona za maufulu a ana la *UN Convention on the Rights of the Child (CRC)* silifotokoza mwachindunji mawu akuti kupeza chilungamo kapena kupeza njira zina zothandizira, mfundo imeneyi ikutchulidwa ndi kufotokozedwa bwino mu mfundo ndi ndondomeko zake; ufulu wa ana wolandira ndi kupeza uthenga wothandiza, ufulu woyankhula maganizo awo, ufulu womvedwa akayankhula; ufulu wotetezedwa ku nkhasa za mtundu uliwonse; maufulu osiyanasiyana, kutetezedwa, komanso kutsimikizira kuti ana amene achita zinthu zophwanya malamulo ndi otetezeka; komanso malamulo oyenera kutsatidwa ngati zapezeka kuti ufulu wa ana waphwanyidwa komanso kuthandiza ana omwe anachitiridwa nkhanza kuti ayambenso kukhala moyo wabwino, ndi zina;
2. Chikalata Chapadziko Lonse cha Ufulu Wachibadwidwe wa Anthu (UDHR) komanso mgwirizano pa nkhani ya maufulu okhudza za ndale, *International Covenant on Civil and Political Rights*, komanso zomwe zili m'zikalata zina, zimakhudzanso ana onse, ndipo zimafotokoza kuti munthu wina aliyense amene ufulu wake waphwanyidwa ali ndi ufulu wotsatira ndondomeko yoyenerera kuti athandizidwe, ndipo izi zichitike kudzera ku

mabwalo a milandu, ku boma, kapenanso ma bungwe ena omwe ali ndi mphamvu pa nkhani za malamulo mogwirizana ndi malamulo amene amatsatidwam'dziko;

3. Mfundo yoti pasakhale kusankhana ndi yofunika kwambiri pa mfundo za CRC ndipo ndi maziko a mfundo za malamulo ambiri pa dziko lonse la pansi, m'zigawo, kapena m'mayiko;
4. Mayiko omwe ndi ma membala abungwe la UN pa msonkhano waukulu wa *UN General Assembly* adavomereza kuti pasamakhale kusiyana pa nkhani yopeza chilungamo chifukwaumenewu ndi ufulu wofunika kwambiri, kwa aliyense kuphatikizapo ana, komanso kuti kuonetsetsa kuti aliyense akupeza chilungamo ndi kuthetsa nkhanza ndi mfundo zofunika kwambiri zopezeka mu malingaliro a chitukuko chokhazikika a chaka 2030, makamaka mu Cholinga cha 16;
5. Ana akukakamizidwa kusenya udindo wobwera chifukwa cha zolephera za anthu m'madera awo, kuphatikizapo nkhanza zosiyanasiyana zomwe amakumana nazo. Zimenezi zimakhudza kwambiri ana osalidwa komanso kusokoneza ntchito yopewa ndi kuthana ndi zinthu zomwe zimapangitsa ana kuti akumane ndi lamulo m'mabwalo a milandu, pena ngati olakwa, kapena oganiziridwa kuti achita choipa, ngati mboni, kapenanso ngati zonse, kapena mu njira ina iliyonse;
6. Mliri wa COVID-19 waonjezera mavuto okhudza kusiyana kwa anthu m'madera ndipo wafooketsanso nthambi zofooka kale zoonza chilungamo ndi chitetezo cha ana. Mavutowa akukolezeredwanso ndi mavuto ena ambiri, monga kuwonongedwa kwa zachilengedwe ndi kusintha kwa nyengo, mikangano ya mayiko, mavuto a zachuma ndi mavuto ena adzidzidzi, omwe amafunika kukhala ndi ndondomeko zabwino komanso zokhalitsa zothanirana nawo zomwensho zingathandize kuonetsetsa kuti ana onseakupeza chilungamo;
7. Pa dziko lonse lapansi, ana ndi achinyamata akutsogolera magulu pofuna chilungamo chokuhdza anthu onse, kusiyana pakati pa amuna ndi akazi, mitundu ya anthu, nyengo ndi chilengedwe komanso nkhani za ndale, ndiponso kutsogolera mitsutso yomwe ikuthandiza kusintha zinthu ngakhale pa nkhani za chilungamo;
8. Kusapezeka kwa vuto la kusankhana mu nthambi zoonza chilungamo cha ana komanso mu ntchito yothandiza ana kupeza chilungamo kudzapindulira ana onse, mosayang'ana kuti iwo ndi ndani, komwe amachokera, komanso momwe moyo wawo ulili;
9. Ana omwe akhudzidwa ndi lamulo pofika ku mabwalo a milandu ali ndi ufulu wofanana ndi mwana aliyense. Zimenezi zikutanthauza kuti ufulu wawo ukuyenera kulemekezedwa komanso kutetezedwa, poyang'anira zofooka ndi zosowa za mwana aliyense komanso pozindikira kuti kuthekera kwao pochita zinthu kukusintha;
10. Ndi zofunika kwambiri kuti ndondomeko zotsogolera nkhani za chilungamo, chitetezo ndi umoyo wabwino wa ana, maphunziro, thandizo la chipatala loyenera ndi zina zotero, zizitsata mosasankha pothandiza ana omwe akhudzidwa ndi lamulo mu njira iliyonse;

Ikulemekeza mauthenga otsatirawa ochokera kwa ana ndi achinyamata omwe adasonkhanitsidwa ndi gulu la ana ndi achinyamata pa dziko lonse la *Child and Youth Advisory Group* ku msonkhano waukulu:

11. Ndife gulu la ana ndi achinyamata amene amakonda ufulu wa ana mogwirizana ndi nthambi zoonza zachilungamo. Zili choncho chifukwa ambiri mwa ife zimenezi zinatichitikirapo, ndiye kuchokera pa zimenezo, tikuona kuti:
 - a. Kusalidwa potengera kusiyana kwa mibadwo komanso kapezedwe kosiyana pa chuma ndi kumene kumapangitsa kuti ana aphwanye malamulo;
 - b. Ana omwe aphwanyanya malamulo kapena amene munthu wina wawachitira zinthu zophwanyanya malamulo amakumana ndi mavuto ambiri, monga nkhanza za pa khomo, nkhanza za m'banja mwawo, komanso kuchotsedwa sukulu, zomwe zingawasokoneze kwambiri maganizo;
 - c. Ndongomeko za malamulo ndi chilungamo siziyika patsogolo maufulu a ana, zomwe zimachititsa ana ambiri kuona ngati akupondereredwa, kusaganiziridwa, komanso kuvutika m'maganizo pamene apezeka m'malo a malamulo;
 - d. Malamulo othetsa umbava ndi umbanda kawirikawiri amatsindika za kupereka chilango komanso kupeza kuti wolakwa ndani, m'malo mothandiza munthu amene walakwitsa kuti asinthe moyo wake komanso kukhazikitsa mtendere;
12. Tikukhulupirira kuti ana ndi nzika zalero komanso atsogoleri a mawa, ndipo tikupempha kuti anthu akuluakulu adziwe izi komanso athandize ana kuti adziwe maufulu awo;
13. Pofuna kuti zinthu zisinthedi kwa ana amene apezeka m'mabwalo opereka chilungamo, tikupempha boma komanso mabungwe kuti agwire ntchito limodzi ndi ana komanso achinyamata pofuna kuonetsetsa kuti maufulu a ana onse, monga momwe malamulo a pa dziko lonse amanenera, akukwaniritsidwa kwa mwana aliyense padziko lonse;
14. Mwapadera, tikupempha izi:
 - a. Ana onse akhale ndi mwayi wochitiridwa chilungamo mofanana mu njira yoganzira aliyense komanso yosasankha pa chifukwa chilichonse;
 - b. Ana apatsidwe ufulu woyankhula maganizo awo ndipo zimene ayankhula zionedwe kuti ndi zofunikira kwambiri;
 - c. Anthu alemekeze kuthekera kwa ana kopanga zisankho zokhudza moyo wao, ndiponso anawo athandizidwe mokwanira ndi achikulire;
 - d. Ana apatsidwe uthenga ndi upangiri woyenera pa momwe angathanirane ndi zinthu zodza mwadzidzidzi komanso zovuta, mofanana ndi momwe ziliri mu nyengo ino ya mliri;

- e. Ana omwe aphwanya malamulo atengedwenso ngati anthu, maufulu ao alemkezedwe, komanso athandizidwe mwathunthu ku mbali ya maganizo ndi umoyo wao;
 - f. Achinyamata amene angochoka kumene ku umwana ndipo aphwanya malamulo, athandizidwe ngati ana;
 - g. Ana ndi achinyamata apatsidwe mwayi wophunzira ndi kutenga nao mbali pa ntchito yosintha moyo wao kuti ukhale wabwino;
 - h. Ana ndi achinyamata athandizidwe kuonetsetsa kuti maufulu awo sakuphwanyidwa, zomwe ndi zofunika kwambiri pa ntchito yobwezeretsa chikhulupiriro mu nthambi zoonza za chilungamo.
15. Tikukhulupirira kuti chilungamo chenicheni kwa ana chingapezeke pamene ana onse akuonedwa mofanana komanso akupatsidwa mwayi wogwirira ntchito limodzi ndi akuluakulu pofuna kukwaniritsa malonjezo okhudzana ndi maufulu;

Choncho, ifeyo monga okonza, abwenzi komanso otenga nawo mbali pa msonkhano wa dziko lonsewu, tikulimbikitsa onse okhudzidwa, kuphatikizapo maboma, ndi mabungwe, kuchita izi:

Chilungamo chenicheni kwa ana, lero ndiponso mawa

16. Ana komanso akuluakulu agwirire ntchito limodzi pofuna kuti chilungamo cha ana chosankha ndi choganizira aliyense chitheke pa dziko lonse. Ntchitoyi igwirike mu njira yoganzira ana ngati akatswiri ndi anthu ofunikira pofuna kusintha zinthu, monga kukonza mfundo ndi malamulo othandiza ana kupeza chilungamo, kukonzanso malamulo omwe alipo kale, kuonanso ndondomeko za mmene malamulowo amagwirira ntchito, kuona ngati pali ogwira ntchito okwanira, ndiponso kuonetsetsa kuti anthu onse m'madera amene tikukhala komanso m'mayiko ali ndi udindo woyankhapo pa ntchito yawo;
17. Kukonza zinthu kuti ufulu wa ana ngati eni maufulu athe kusintha zinthu, komanso kuthandiza kuti mawu a lero ndi mawa amveke patali. Izi zingatheke popereka uthenga wogwirizana ndi ana komanso wosankha pa nkhani ya malamulo ndi njira zopezera thandizo lokhudza malamulo, pokoza momwe anthu amamvera za maufulu a ana, pokhazikitsa njira ya kulumikizana yokomera ana komanso popereka mpata kwa ana ochokera m'manja ndi m'madera osiyanasiyana otenga nawo gawo pa zochitika zosiyanasiyana, kuphatikizapo ana omwe aphwanya malamulo;
18. Kukhazikitsa kuti kutenga nawo mbali kwa ana kuyikidwe m'malamulo komanso kulola lamuloli kuti ligwire ntchito pofuna kuonetsetsa kuti ana akukhala nawo pa zokambirana, m'malo mongolimbikitsa kuti ana azitenga nawo mbali pa zochitika, komanso kungowafunsa maganizo awo kumbali, makamaka ana amene aphwanya malamulo kapena amene alakwiridwa, amene kawirikawiri amayiwalidwa pa zokambirana chifukwa cha kusalana, kusankhana komanso momwe zinthu ziliri pa moyo wawo;

Kupereka mpata woti aliyense apeze chilungamo cha ana popanda kusankhana

19. Mfundo ya kusankhana ndi kusalana ikhale yayikulu pa zokambirana zilizonse zofuna kusintha zinthu pa nkhani yokhudza chilungamo kwa ana, ndipo pakhazikitsidwe njira zothandiza kuthana ndi kusankhana pa chifukwa chilichonse, makamaka kwa ana amene aphwanya lamulo kapena amene alakwiridwa. Zimenezi zichitike mu njira yomwe sipangitsa kuti anawo atchulidwe mayina achipongwe komanso kutengedwa ngati anthu a mtundu wina;
20. Kutsimikizira kuti ana onse akupeza mwayi wofanana wolandirira chilungamo, makamaka ana ochokera m'magulu amene amasalidwa. Izi zichitike mu njira yoganizira chilungamo chokhudzana ndi malamulo oletsa umbanda, oyendetsera zinthu m'dziko, okhudza chikhalidwe, ndiponso nkhani zina zochitika m'madera;
21. Kukonza ndondomeko zokhudza chilungamo zokomera anthu a misinkhu yonse, omwe ali ndi ulumali, zogwirizana ndi amuna ndi akazi omwe, ndiponso zolemekeza ufulu wopeza chilungamo kwa ana onse amene aphwanya lamulo kapena amene alakwiridwa. Ndongomekozi zikhale zogwirizana ndi momwe anawo alili, zothandiza kuti anawo akule bwino, komanso akhale ndi makhalidwe labwino;
22. Kukhazikitsa njira zolemekezera ndi kuganizira chikhalidwe ndi chiyankhulo cha mwana aliyense amene waphwanya lamulo kapena amene walakwiridwa;
23. Kukhazikitsa ntchito za m'madera komanso njira zosakhudza ndende zothandiza kuti ana amene aphwanya lamulo athandizidwe bwino, zopangidwa ndi anthu a m'dera lomwero komanso zopezeka kwa ana onse moganizira aliyense ndi mosasankha;
24. Kupitiriza ndi kulimbikitsa kutolera uthenga kudzera mukafukufuku m'mayiko ndi m'zigawo pofuna kumvetsa bwino momwe ana ochokera m'magulu ang'onoang'ono komanso osalidwa amaphwanyira malamulo kapena kulakwiridwa, momwe amalandirira chilungamo komanso magwero a chisamaliro choipa;
25. Kuthandiza atsogoleri-a ndale kuti ayikepo mtima pa nkhani yokonza malamulo othandiza kuti ana onse alandire chilungamo mopanda kusalidwa. Izi zidzatheka povomereza kuyikapo ndalama ndi nthawi yokwanira komanso kuyankhula ndi atengambali omwe ntchito zawo zimakhudza ana;

Kuthandiza ana kuti apeze chilungamo pa nthawi yamavuto monga miliri.

26. Kuvomereza malamulo ndi mfundo zothandiza kuti ngakhale pa nthawi ya mavuto chilungamo chipezeke kwa ana, pofuna kuti mwayi woti ana apeze chilungamo ukhalepobe;
27. Kuganizira zokhazikitsa mabwalo a milandu, kuzenga milandu komanso misonkhano ina pogwiritsa ntchito njira za zamakono monga intaneti, potsatira ndondomeko zonse zomvetsera mlandu. Koma izi ziyenera kuchitika mu njira yotetezeka komanso yosunga chinsinsi mofanana ndi momwe zimakhaliira. Choncho padzafunika kuganizira njira

zamakonozi m'madera osiyanasiyana, popanda kusalana, mosunga chinsinsi, komanso molemekeza ufulu wa mwana, ndipo zimenezi ziyenera kuchitika pokhapokha ngati mwanawo wavomereza ndipo akugwirizana ndi ndondomeko zonse;


28. Kukhazikitsa ndi kutsatira ndondomeko zomveka bwino zotsogolera mgwirizano wokhudza mbali zosiyanasiyana pa nthawi ya mavuto adzidzidzi kapena mliri, ndi kuonetsetsa kuti mabungwe ndi anthu amene ali ndi udindo waukulu wosamalira ana komanso malamulo otetezera ana aganiziridwe popereka thandizo pa nthawi yovutayi;
29. Kukonza ndondomeko yothandiza kuti okhudzidwa pa nkhani yopereka chilungamo alandire maphunziro oyenerera owakonzekeretsa kuthandiza mwachangu komanso mu njira yabwino komanso kuti agwiritse bwino ntchito zipangizo zonse zofunikira;
30. Kulemba malangizo okhudza mliri, ogwirizana ndi ana, mosayang'anira kuti munthu ndi mwamuna kapena mkazi, ndiponso othandiza kwa anthu amene ali ndi ulumali. Malangizowa ndi ofotokoza njira zothandiza kupirira ndi kuthana ndi mavuto mgwirizana ndi mafulu a ana komanso mwayi wopeza chilungamo;

Mwayi wopeza chilungamo wokomera ana kwa ana onse amene aphwanya lamulo kapena amene alakwiridwa

31. Kupeza njira zosiyanasiyana zothandiza kuti ana apeze chilungamo mosavuta podzera kwa anthu ndi mabungwe osiyanasiyana otenga nawo gawo, mu njira imene ingathandize kuchepetsa zoti ana aziphwanya lamulo kapena kulakwiridwa;
32. Kupereka chilungamo ndi zithandizo zina zoyenera ndi zogwirizana ndi ana kwa ana onse amene aphwanya lamulo kapena alakwiridwa, mosayang'ana kuti munthu ndi mwamuna kapena mkazi, othandiza kwa omwe ali ndi ulumali, komanso ogwirizana ndi msinkhu wa anawo. Izi zikuyenera kuperekedwa mu njira imene ingathandize ana omwe akukumana ndi mavuto, moganizira komwe amachokera, momwe zinthu zilili pamoyo wawo, komanso kukhwima kwawo mu nzeru;
33. Kutsimikizira kuti ana omwe aphwanya lamulo kapena alakwiridwa akulandira thandizo kuchokera kwa akatswiri odziwa zachipatala pofuna kuwathandiza pa nkhani ya maganizo komanso kuwathandiza kuti akwanitse kupirira mavuto omwe adakumana nawo;
34. Kufufuza ndi kupeza njira zimene zingathandize ana omwe aphwanya lamulo kapena alakwiridwa pofuna kuti asabwerezenso kuchita zolakwikazo, komanso pofuna kuwathandiza kuti ayambe kukhala moyo wabwino, wopanda ziwawa ndi mavuto ena. Kutu izi zitheke, maanja akuyenera kuthandizidwa kudziwa zoyenera kuchita mwana akayamba kumene kuchita zinthu zophwanya lamulo ndi kumuwongolera kuti asinthe khalidwelo;
35. Kuyika patsogolo njira zothandizira ana omwe anaphwanya lamulo kapena kulakwiridwa kuti apeze chilungamo, thandizo losintha moyo wawo, kuyambiranso kukhala pakati pa anthu onse. Kutu izi zithekepakufunika ndondomeko zabwino zothandiza anawo, m'malo motsatira njira zimene zimachititsa kuti ana asalidwe komanso aonedwe ngati oipa;

36. Kuyika njira zothandiza kuti makhalidwe ena a ana asamatengedwe ngati milandu, makhalidwe amene angathetsedwe ndi mbali zokhudzidwa ndi nkhani ya chitetezo cha ana, a zaumoyo, komanso opereka thandizo lokhudza kaganizidwe, ndi ena monga njira zosiyanasiyana zothanirana ndi milandu yokhudza mankhwala ozunguza bongo; komanso
37. Kukhazikitsa maphunziro apadera komanso kukonza ndondomeko yamaphunziro yogwirizana ndi zaka zinozi yomwe ilipo kale pofuna kukhazikitsa gulu la anthu odziwa kugwira ntchito monga okhudzidwa, apolisi, oweruza milandu ndi ena pa nkhani yokhudza chilungamo ndi chitetezo cha ana. Maphunzirowa akufunika kukhala okhudza mbali zosiyanasiyana monga kumvetsa bwino mmene mwana amakulira, njira zabwino zofunsira mafunso ana, ndondomeko yabwino yothandiza kuti ana asamachite mantha, komanso njira zothetsa kupondereza ndiponso kusala ana.

**Omwe
Akugwiriz
ana ndi
Mfundo za
M'chikalat
achi**



Ndondomeko ya **Global Initiative on Justice With Children** inapangidwa ndi mabungwe angapo omwe amagwira ntchito m'mayiko osiyanasiyana amene amachititsa misonkhano ya dziko lonse, *World Congresses as a Justice With Children Global Milestone*, komanso amalimbikitsa anthu ndi mabungwe ogwira ntchito zosiyanasiyana pogwiritsira ntchito pulogalamu ya pa intaneti ya bungwe loona za chilungamo la *Justice With Children*. Cholinga chake ndi kuyendetsa zokambirana pakati pa akatswiri osiyanasiyana kudzera m'misonkhano yochitika pa intanet komanso pamaso pofuna kuunikira ndi kugawana nzeru zokhudza chilungamo cha ana.

Misonkhano ya Pa Dziko Lonse Yokhudza Kuchitira Chilungamo Ana **imakonzedwa** pofuna kuthana ndi mavuto okhudza ana omwe aphwanya lamulo kapena omwe alakwiridwa. Misonkhanoyi imapereka mwayi kwa ana ndi achinyamata, kwa akatswiri opanga mfundo zoyendetsera boma, akatswiri a maphunziro, ogwira ntchito m'boma, oyimira bungwe la UN ndi akatswiri ena kuti achite zotsatirazi: (1) Kulimbikitsa ndondomeko zoyenera ndi zosakondera zokhudza chilungamo cha ana pa dziko lonse; (2) Kupereka mwayi kwa akatswiri osiyanasiyana kuti akambirane ndi kugawana nzeru, alimbikitse kugwira ntchito limodzi, akonze mfundo ndi malamulo, komanso adziwitse ena za chilungamo cha ana; ndiponso (3) Kuthandiza kukhazikitsa malamulo ndi mfundo za dziko lonse lapansi zokhudza maufulu a ana ndi achinyamata amene aphwanya lamulo kapena amene alakwiridwa.

Msonkhano Wa Pa Dziko Lonse wa Chaka cha 2021 Wokhudza Kuchitira Chilungamo Ana **unatsindikapa** njira zabwino pofuna kuchepetsa kusalana kumene kumasokoneza mwayi wozeza chilungamo komanso chilungamo choyenera, pofunanso kuonetsetsa kuti ana onse akuonedwa mofanana pa nkhani yokhudza lamulo. Anthu otenga nawo mbali pa msonkhanowu adachita zokambirana za mayiko ndi zigawo zonse kuphatikizapo misonkhano yofunsa ndi kuyankha mafunso, maphunziro ndi misonkhano ya m'magulu. Mogwirizana ndi mutu waukulu wakuti "Kuonetsetsa kuti ana onse akuchitiridwa chilungamo: kukonza zoti ana asamasalidwe komanso kuti ena azitenga nawo gawo pankhani zochitira chilungamo ana". Mitu ing'onoing'ono khumi ndi umodzi (11) yotsatirayi idakambidwa kwambiri pa msonkhanowu:

- Kusolidwa kwa ana komanso kuonedwa ngati olakwa makamaka ana ochokera ku mtundu wa anthu a kumudzi ndi magulu ena a anthu ochepa;
- Kusolidwa potengera kuti ndi mwamuna kapena mkazi, zosankha zake pa nkhani zogonana, zosankha zake pa nkhani yosintha n'kukhala mwamuna kapena mkazi: zimenezi zimathandiza kuonetsa njira yomwe ikutsatidwa pa nkhani ya chilungamo chokhudza mwamuna kapena mkazi;
- Kusolidwa kwa ana ndi achinyamata omwe akhudzidwa ndi kuchoka kudziko la kwao, kuphatikizapo othawa kwao, ana opezeka ku dziko lina popanda makolo awo, ndiponso ana amene makolo awo anachokera ku dziko lina;
- Kusolidwa chifukwa cha ulumali ndiponso mavuto ena okhudza umoyo wawo;
- Kusolidwa chifukwa chogwiritsira ntchito mankhwala ndi zinthu zina kapenanso chifukwa chogwiritsira ntchito mankhwalawa molakwika;
- Kuona kuti ana ndi olakwa potengera zimene amachita pa intaneti;
- Milandu yopalamulidwa chifukwa chosatsatira mlingo wa zaka zakubadwa komanso potengera momwe munthu alili.
- Kuonetsetsa kuti mawu a ana akumvedwa mu dongosolo lolimbikitsa chilungamo;
- Kuonetsetsa kuti maufulu a ana ukulemekezidwa m'malo omwe amagwiritsa ntchito ndondomeko za malamulo zambiri;
- Kukonza ndondomeko za chilungamo cha ana zokhazikika pa nthawi ya miliri; komanso
- Kuthana ndi nkhanza zopezeka m'malo olimbikitsa chilungamo cha ana ndiponso kuonetsetsa kuti pali njira zabwino zothandizira ana alakwiridwa, aphwanya lamulo, ndiponso pa nthawi imene anawo ali mboni pa mlandu.

Chikalata cha Padziko Lonse Chokhudza Kuchitira Chilungamo Ana chidalembedwa ndi a *World Congress Consortium* ndi nthambi yake yotchedwa *Child and Youth Advisory Group*, pogwiritsa ntchito maganizo ochokera ku bungwe la akatswiri a sayansi *Scientific Committee*, ma bungwe ena, komanso anthu amene adachita nawo msonkhano wa *World Congress* ndi misonkhano ina yokonzekera msonkhano umenewu.

Kuti mudziwe zambiri, pitani pa www.justicewithchildren.org.